# UTHENGA WABWINO WOLEMBEDWA NDI MARKO

# KUKAMBA ZA MOYO NDI MACHITIDWE A YESU KHRISTU




**Ndemanga za baibulo zothandiza munthu kuphunzira pa yekha kapena pa gulu**

**Lolembedwa ndi Fred Morris**
**Zatathanzidwa ndi Jones Chamangwana**

## Marko Gawo 1

## Mutu 1 mpakana 8

Manna Publications

## Kwa Wowerenga kapena Mtsogoleri

Ndemanga zimenezi zimathandiza kufotokoza Baibulo m'njira yosavuta kuwerenga ndi kumvetsa. Ndiwosavuta kumasulira. Mukhoza kugwiritsa ntchito mabukuwa pophunzira Baibulo panokha kapena ndi anthu ena pagulu. Aliyense ayenera kukhala ndi buku lake komanso Baibulo ngati n'kotheka.

**Kambiranani izi:** Pamene mukuwona izi, pali mafunso oti mudziyankhe mwapemphero kapena kukambirana mu phunziro la gulu. Zimathandizanso wowerenga kukumbukira mavesi a m'Baibulo.

**Mabokosi ophunzitsira olamuliridwa:** Kumene mumawaona, mfundozo zimapereka chiphunzitso chowonjezereka cha moyo panthaŵi imene ndime ya m'Baibulo inalembedwa ndipo imatithandiza kugwiritsira ntchito chiphunzitsocho masiku ano.

**Mau Otsogolera:** Mawu a m'Baibulo, otengedwa mu HOLY BIBLE New International Reader's Version, ndi ovomerezeka © 1996, 1998 by International Bible Society. Inaperekedwa panthawiyo ndi chilolezo cha Hodder & Stoughton Ltd., membala wa Hodder Headline Group. Maumwini onse ndi otetezedwa. Onani pa intaneti pa: www.biblestudytools.com/nirv

Zithunzi ndizovomerezeka © Global Recordings Network (GRN). Kugwiritsidwa ntchito ndi chilolezo.

---

**Mark Part 1 Manna Bible teaching commentary © 2001 Fred Morris, Manna Publications (USA) Inc. All rights reserved.**

**Mulungu watithandiza kusindikiza mutu umenewu m'mayiko otsatirawa:**
***Revised Worldwide English edition first published in the UK in 2001***
Reprinted 2001: Kenya (English).
Reprinted 2002: India (Tamil), Uganda (English), Kenya (Swahili), Sudan (Dinka).
Reprinted 2003: Swaziland (English), Malawi (Chichewa), Kenya (Bari for Sudan), Uganda (English), Ethiopia (Amharic).
Reprinted 2004: Kenya (English, Swahili), Pakistan (Urdu), Uganda (English).
Reprinted 2005 revised edition: Myanmar (English, Khumi Chin), Liberia, Uganda (English)
Reprinted 2006: Zambia, Liberia, Tanzania, Sierra Leone (English), Myanmar (Mizo Chin)
Reprinted 2007: Ghana for Niger, Burkina Faso (French), Ghana for Niger (Hensa), Nigeria, Kenya, Uganda (English), Burundi (Kirundi), People's Rep. Congo (French)
Reprinted 2008: Liberia (English), Togo (French)
Reprinted 2013: Malawi (Chichewa)
Reprinted 2015: Malawi (Chichewa, including Braille)
Reprinted 2016: Malawi (Chichewa)
Reprinted 2017: Sierra Leone (English)
Reprinted 2018: Equatorial Guinea (Spanish)
Reprinted 2019: Malawi (Chichewa)
Reprinted 2021: Malawi (Chichewa)
Reprinted 2022: Malawi (Chichewa)
Reprinted 2023: Malawi (Chichewa), Mozambique (Chichewa)
Reprinted 2024: Malawi (Chichewa, English)

# Marko Gawo 1 Mutu 1 mpakana 8

# UMBONI WA MARKO PA UTHENGA WA BWINO WA YESU KHRISTU

Uthenga wabwino wolembedwa ndi Marko ukupezeka pa bukhu la chiwiri mwa mabukhu anayi onena za moyo wa Yesu Khristu. Yohane Marko adalemba bukhuli pakati pa zaka za 42 AD ndi 44 AD zimene iye adamva kuchokera kwa (Petro). Nkhaniyi idachitika mu Yudeya ndi mu Galileya, dziko limene lero likutchedwa Israel. Bukhu la Marko limatiuza zinthu zambiri zokhudza sabata yotsiliza, Yesu asanakhomeredwe pamtanda.

Bukhuli limathera pamene Yesu anauka kwa akufa ndi kukwera kupita kwa Atate ake kumwamba. Machaputala asanu ndi atatu oyambirira a uthenga wa Marko akutiuza za kuphunzitsa ndi kuchiritsa kwa Yesu poyamba pa ntchito yake. Uthenga wa bwino ndi woti Mulungu amatikonda kwambiri, kotero kuti anatuma mwana wake Yesu kudzatifera ife pamtanda imfa yowawa ndi yomvetsa chisoni. Izi zitanthauza kuti aliyense amene apembedza Mulungu ndikukhulupirira Yesu Khristu, ali nawo moyo wosatha.

## KODI MARKO ANALI NDANI?

Yohane Marko anali mu Yuda koma analibe dzina la pfuko la Chiyuda "Marko". Lyeyu adamva zambiri za Yesu kuchokera kwa Petro, m'modzi mwa ophunzira a Yesu. Petro anali kumkonda Marko, kotero kuti anali kumutchura kuti "mwana wanga" (1 Petro 5:13).

Mayi wa Marko anali ndi nyumba yayikulu mzinda wa Yerusalemu. Mayiyu adamva za uthenga wabwino wa Yesu Khristu, ndipo anakhulupirira. Chotero akhristu ena anali kusonkhana ndi kupembedza Mulungu ku nyumba kwawo (Machitidwe 12:12).

Kwa nthawi yayitali mtundu wa Chiyuda unayembekezera mpulumutsi. Mesiya wolonjezedwa ndi Mulungu. Ayudawa anali kuganiza kuti Mesiyayu adzawapulumutsa m'manja mwa adani awo, Aroma amene anali kuwalamulira. Atsogoleri azipembedzo ambiri anali ndi ophunzira awo amene amatha kusiya ntchito zawo kutsatira mtsogoleriyo, kuti aziwaphunzitsa. Marko adatsatira Petro amenenso adatsatira Yesu. Marko adamva Petro akunena za Yesu ndi zomwe iye adachita. Marko wachichepereyo adakhulupirira kuti Yesu anali Mesiya wolonjezedwayo. (Khristu Ambuye).

Marko anali msuweni wa Barnaba, bwenzi la Paulo, ndipo anayendanawo awiriwa, kuphunzitsa uthenga wabwino ku Asiya (Turkey). Atasiyana nawo Marko anabwerera ku Yerusalemu. Paulendo wotsatira, Paulo sanafune kuyendanso ndi Marko. Chotero Barnaba anatengana ndi Marko napita ku Kupro. Kenaka, paulo ndi Marko adayanjananso. Paulo adalemba kalata ali mundende kufotokoza za Marko Kuti "akundikhalira ine chotonthoza mtima" (Akolose 4:11).

Marko analemba za Yesu Khristu kuti anali mwana wa Mulungu koma Iye mwini anali kudzitchula yekha "mwana wa munthu". Ili ndi dzina limene Mulungu mwini analipereka kwa aneneri kalelo amene anatumikira pa dzina lake (Ezekiele 12:2) koma mbukhu la Marko tikumva kuti Yesu anali mwana wa Mulungu (Marko 1:11; 9; 7)

**Kambiranani izi:**

1. Mukudziwapo chayani zokhudzana ndi Marko?
2. Kodi Marko anamva kwa ndani za Yesu?
3. Yesu asiyana bwanji ndi aneneri ena onse?

## KODI MARKO ADAMUFOTOKOZA YESU MOTANI?

Dongosolo la Mulungu ndi lodabwitsa kwambiri, Iye anasankha namwali wina dzina lake Maria kuti mpulumutsi abadwe Luke 1, 26-35; 2; 1-20). Marko akuyamba uthenga wake potiwuza za Yesu atafika zaka makumi atatu; Iye adadza kudzachita ntchito za Mulungu Atate, kudyetsa anjala (Marko 8:1-13), kuchiza odwala (2:1-12), kutulutsa mizimu yoipa (9:14-32) kuukitsa akufa (5:42) Zizindikiro izi zinali kutsimiza kuti Yesu analidi wotumidwa kuchokera kwa Atate(Yohane 1:42). Marko amafuna kutitsimikizira kunena kuti Yesu anali mwana wa Mulungu. Iye ndiye Uthenga wabwino wa chipulumutso cha machimo kwa iwo amene amukhulupilira Iye.

Baibulo limanena kuti pakuti, onse anachimwa (Aroma 3:23). Chifukwa chakuti tinabadwa mu zoipa, Mulungu anatumiza Mwana wake wobadwa yekha kudzatiombola ife ku machimo. Chithu chachikulu chimene Yesu anachita ndi kulolera kufa mmalo mwa dziko lonse. Iye amene analibe mtchimo koma anasenza mtchimo m'malo mwathu. Ife tinayenera kufa chifukwa cha machimo koma Iye analolera kufa m'malo mwathu kuti Mulungu atikhulukire machimo athu. Zithu izi zinayamba kuyakhulidwa zaka zambiri zapitazo Yesu asanabadwe.

## MASIKU OYAMBILIRA A YESU PA DZIKO LAPANSI

Mateyu 1 & 2, Luka 1 & 2 komanso Bukhu la Yohane timamva zambiri ya kubadwa kwa Yesu.Timamvanso za Yohane m'batizi zithu zimene mbukhu la Marko sizinalembedwemo.

Ulamuliro wa Chiroma unali ponse ponse panthawi imene Yesu amabadwa. Ndipo kunali masiku aja kuti lamulo linatuluka kwa Kaisara Augusto kuti dziko lonse lokhalamo anthu lilembedwe (luka 2; 1). Iye anali kufuna kudziwa chiwelengero cha Ayuda okhala mu Israeli.

## Zithu makumi awiri onenelatu za Mpulumutsi

Mchipangano cha kale zomwenso zinatsimikizidwa ku chipangano cha tsopano.

Pali maumboni ambiri amene tingathe kuwapeza mu chipangano chakale ndi chatsopano. Marko yekha tipeza makumi asanu pamene Mateyo makumi asanu ndi anayi.

1. Yesu Mesiya wolonjezedwa. mwana wa Mulungu amene ali Ambuye kuchipangano chakale Deuteronomo 18:15; Yeremiya 23:5; Yesaya 53:12. Kuchipangano chatsopano Mateyu 16:16; Marko 1:11; Luka 2:11; Ahebeli 7:25.)
2. Yesu olonjezedwa mchilitsi (Yesaya 35:5, 6; Marko 2:12; 7:35; 8:25.)
3. Yesu wa mfuko la Davide. (Yesaya 9:7; Mateyo 1:1.)
4. Mulungu alonjeza Abrahamu kuti dziko lonse lidzadalitsika mwa Iye (Geneses 18:18; Mateyo 1:1; Machitidwe 3:25.)
5. Yesu anabadwira ku Betelehemu mu mzinda wa Yudeya (Micah 5:2; Mateyu 2:1.)
6. Yesu anabadwa kwa Namwali amene anali asanadziew mamuna (Yesaya 7:14; Mateyo 1:18.)
7. Yesu ali mwana anathawira ku Aigupto, pamene Herodi anafuna kupha mwanayo (Hoseya 11:1; Mateyu 2:14, 15.)
8. Yesu anayenda mu Galileya monse ndikuphunzitsa za uthenga wabwino (Yesaya 9:1, 2; Mateyo 4:13, 14.)
9. Yesu anali mneneri woposa wonse wonenedwa ndi Mose (Deuteronomo 18:15; Yohane 6:14; Machitidwe 3:22.)
10. Yesu, Wamsembe wamuyaya amene amakhulukukira machimo, Yesu ndi wachifundo chosatha (Yesaya 11:2; Luka 2:52.)
11. Abale a Yesu sanakondwere naye (Yesaya 53:3; Yohane 1:11.)
12. Yesu alowa mu Yerusalemu atakwera pa bulu (Zechariya 9:9; Mateyo 21:2-9 ndi Yohane 12:12-16.)
13. Yesu adzapelekedwa ndi mmodzi mwa akuphunzira ake (Masalimo 41:9; Marko 14:10, 18-20.)
14. Yesu adzagulitsidwa ndi ndalama za siliva makumi atatu (Zechariya 11:12; Mateyo 26:15.)
15. Mwa Yesu munalibe chinyengo chilichonse (Masalimo 27:12; Mateyo 26:59-61.)
16. Yesu sanayankhe kanthu pamene anamunenera zoipa zilizonse. (Yesaya 53:7; Mateyo 26:62, 63.)
17. Yesu anamupachika pamodzi ndi wochita zoipa (Yesaya 53:12; Mateyo 27:38.)
18. Anagawana zovala za Yesu pa mtanda (Masalimo 22; 16-18; Zekalia 12; 10; Yohane 19; 23.)
19. Yesu anamuboola manja ndi mapazi ake (Masalimo 22:16; Yohane 19:37; 20:27.)
20. Yesu ali pamtanda anthu anamuseka ndi kumunenera zinthu zoipa (Masalimo 22:6-8; Mateyo 27:39, 40.)

Ndipo onse anatuluka kukalembedwa munthu aliyense kuchokera mu midzi yawo ndipo Yosefe yemwe anakwera kuchokera ku Galileya ku mudzi wa Nazarete kunka ku Yudeya ku mudzi Davide dzina lake Betelehemu chifukwa Iye anali wa banja ndi mfuko lake la Davide kukalembedwa Iye mwini pamodzi ndi Maliya wopalidwa naye ubwenzi ndi uyu anali ndi pakati. Angakhale kuti awiriwa anali asanakhalire limodzi monga banja (Matt. 1:19).

Pochenjezedwa mkulota Yosefe anavomera kumutenga Maliya monga mkazi wake (1:25).

Ndipo panali pokhali iwo komweko masiku ake a kubala mwana anakwanira ndipo Iye anabala mwana wake woyamba namukulunga iye mu msalu namgoneka modyera ng'ombe chifukwa kuti anasowa malo mnyumba ya alendo (Matt. 1:18, 20). Ndipo Mzimu wa Ambuye unali pa iye.

## ANZERU AKUM'MAWA

Mulungu anasankha kuti uthenga wakubadwa kwa Yesu uyambe kufika kwa anthu wamba, abusa ang'ombe. (Luke 2:12). Ndipo mngelo wa Ambuye anati kwa iwo,"musaope pakuti onani ndikuwuzani inu uthenga wabwino wa chikondwelero chachikulu, chimene chidzakhala kwa anthu onse, pakuti wakubadwirani inu mmudzi wa Davide, Mpulumutsi amene ali Khristu Ambuye'. Anthu wamba analandira uthenga wakubadwa kwa Yesu mphulumutsi wa anthu onse kenaka ndi pamene timamva za anzeru akummawa.

Ndipo pa kubadwa kwake kwa Yesu m'Betelehemu wa Yudeya m'masiku a Herode mfumu, onani Anzeru a kum'mawa nafika ku Yerusalemu; nati ali kuti amene anabadwa Mfumu ya Ayuda? Chifukwa tinaona nyenyezi yake ku m'mawa ndipo tadzera kudzamulambira Iye" (Mat. 2:2).

Ndipo Herode Mfumuyo pakumva ichi anavutika ndi Yerusalemu yense pamodzi naye. Ndipo iye anasonkhanitsa ansembe akulu onse ndi alembi a anthu, nafunsira kwa iwo, adzabadwira kuti Khristuyo? Ndipo anamuwuza iye M'Betelehemu wa Yudeya (Mika 5:2).

Kumeneko ndi kumene anthu olemekezeka anakamuonera mwanayo. Yesu anasankha kubadwira malo wamba kumene kunali ku khola la ng'ombe m'mene wina aliyense sanayembekezere kuti mpulumutsi olonjezedwayo angabadwire kumeneko, apa tikuona kuti amzeru aku m'mawa aja anafunsira kwa Herode poyembekezera kuti mwina mpulumutsi wolonjezedwayo ali kumeneko kapena malo ena apamwamba. Koma Herode anakwiya nalamula asilikali ake kupha ana onse akufika zaka ziwiri ndi tating'ono tonse (Mat. 2:16).

Mngero wa Ambuye anawonekera kwa Yosefe mkulota nati, tauka tenga kamwanako ndi amake muthawire ku dziko la Aigupto mukhale kumeneko kufikira nthawi imene ndidzakuwuza, popeza Herode adzafuna kuononga mwanayo (Mat. 2:13; 2:22, 23).

Ndipo mwanayo anakula nalimbika, nakhala ndi nzeru ndipo Chisomo cha Mulungu chinali pa Iye (Luka 2:52) Ndipo Ana ndi Simeoni anawadalitsa.

Koma pomwalira Herode onani m'ngero wa Ambuye anaonekera mkulota kwa Yosefe m'Aigupto nati; tenga kamwanako ndi amake mupite ku dziko la Israyeli chifukwa anafa uja wofuna moyo wa mwanayo. Pamenepo Yosefe anadza nakhazikika mmudzi dzina lake Nazarete kuti chikachitidwe chonenedwa ndi aneneri kuti adzatchedwa "m'nazarayo"

Mu Uthenga wabwino wa Luka timamva za munthu wotumidwa kudzachitira umboni za Yesu dzina lake Yohane M'batizi (Luka 1:5-24; 57-66). Kubadwa komanso moyo wake unali wodabwitsa. Iyeyu anababwa kwa Zakaliya ndi Elizabeti. Mu ndime zotsatirazi Marko atithandiza kufotokoza bwino za munthu ameneyu komanso dongosolo la Mulungu limene analiyika pa Iye.

**Yesu Khristu Monga Mulungu Komanso Ngati Munthu**

Bukhu lopatulika limaphunzitsa za Yesu Ngati Mulungu m'thupi. Iye anali Mulungu nabadwa monga munthu kwa Namwali Maliya. Ndipo monga munthu anakhala pakati pathu koma osachimwa. Mulungu mwini anadzichepetsa nakhala m'maonekedwe a munthu, kubadwa mpaka kukula Ngati mwana wa Maliya. Pamene anapatsidwa mwa Mzimu Woyera. Chifukwa cha ichi Yesu ndi Mwana wa Mulungu wobadwa yekha.

Mau ake ndi Mau a Mulungu wotumidwa kwa Atate, ndipo Iye madziwa mtima wa Mulungu.

Iye mwini anali kukonda kunena kuti mwana wa munthu chifukwa kwa zaka makumi atatu analeledwapo ndi anthu, nadziwa mavuto, kumva njala ndi zina zonse zimene ife anthu timakumana nazo koposa zonse anali kumveranso makolo ake apansi pano, nakhalabe womvera kufikira imfa ija ya pamtanda

## Kambiranani izi:

1. Mngero wa Mulungu anayankhula ndi Zakaliya (Luka 1:13-20), Maria (1:26-38) ndi Yosefe (Matt. 1:20-25). Kodi anthu amenewa analandira bwanji zonenedwazo? Ndipo ife tingaphunzirepo chiyani pa zimenezi?
2. Kodi amzeru aku m’mawa analandira bwanji uthenga wa kubadwa kwa Yesu? Fotokozani mosiyanitsa ndi mmene uthenga womwewu unafikira kwa abusa ang’ombe. Tipange bwanje kuti Mulungu azititsogolera (John 14:26)?
3. Za kubadwa kwa Yesu anthu anazilandira mosiyana kwambiri; mukuganiza kuti anthu awa azilandira motani? Maliya, Mfumu Herode, Amzeru a ku m’mawa ndi abusa aku Betelehemu, panalinso ena Simeoni ndi Anna aku Yerusalemu. Inuyo mukuganiza bwanji za kubadwa kwa Yesu? Ndipo mumati Iye anali ndani?
4. Mukuganiza chanu m’chiyani Mulungu, anatsogoza azineneri komaso Angelo kunena za Yesu (Matthew 1:20-22, 2:6; Luke 1:32-35, 2:10-11)?

## Kuwerenga Baibulo: Marko 1:1-13

## YOHANE M'BATIZI AKONZA NJIRA YA YESU

Mumavesi khumi ndi atatuwa Marko akutiuza za anthu otsatirawa:

- Yohane Mbatizi, wolalikira m'chipululu (1:4)
- Yesu mwana wa Mulungu, wotsika kumwamba nadzabadwa ngati munthu (1:9)
- Mulungu, Mzimu Woyera, amene anadza pa Yesu (1:10)
- Mulungu, Atate, amene anayankhura kuchokera kumwamba (1:11)
- Satana, amene anamuyesa Yesu (1:13)
- (Angelo amene anamutumikira Yesu (1:13)

Yohane M'batizi anawoneka monga m'neneri wa Mulungu mumakhalidwe ake. Analakhura monga wotumidwa ndi Yehova (1:6). Lye adakwaniritsa ulosi wa Yesaya m'neneri zaka mazana asanu ndi awiri za m'mbuyomo. Yesaya anena za mau ofuula mchipululu akunena "Konzani khwalala la ambuye". (Yesaya 40:3)

Marko anagwiritsa ntchito ulosi umenewu kutiuza za Yohane m'batizi (Marko 1:3). Mulungu adam'dzaza Yohane ndi Mzimu wake, asanabadwe, kuti adzagwire ntchito yake. (Luke 1:13, 41). Yohane adadza kudzauza anthu kuti 'Asiye machimo awo ndipo abatizidwe' (Marko 1:4).

Anthu akalasidwa mitima yawo chifukwa cha machimo, ndikutembenuka mtima, Yohane anali kuwabatiza, ubatizo wa mmadzi. Izi zinali chitsimikizo cha kulapa kwawo.

'Kulapa' kutanthauza kumva chisoni chifukwa cha machimo ndikufuna kuwasiya machimowo ndi kubwereranso kwa Mulungu. Machimo ndi chinachirichonse choyipa chimene timaganiza, kumayakhula kapana kuchita.

Uchimo uyimiriranso zinthu zabwino zimene ife timayiwala kuzichita. Uchimo umatirekanitsa ife ndi Mulungu wathu amene ali wabwino ndiponso wangwiro. Chotero kumizidwa m'madzi mu ubatizo ndi njira yosonyeza kuti Mulungu watsuka ndi kuchotsa moyo wathu wakale ndipo tikuyambanso moyo watsopano ndi iye.

Mulungu adalonjeza kupulumutsa ana a Israel kwa adani awo ndi kuwadalitsanso. Iye adalonjeza kuti adzatumiza Mpulumutsi kapena kuti Mesiya. Aneneri ambiri a munchipangano chakale adanenera za Mpulumutsiyu. Zaka zambiri zitadutsa anthu adataya chikhulupiriro. Kenaka Yohane adafika! Iye adadza kudzakonza njira ya Yesu, Mpulumutsi. Yohane sanali Mpulumutsiyo ayi koma adawauza anthu za Yesu. Iye adati wina wamkulu akudza pambuyo panga (1:7, 8). Yesu atafika anali kutsogozedwa ndi ndi Mzimu wa Mulungu ndipo Satana dayesa kuti amuyese koma zinakanika (onani Mateyu 4:3-9).

**Kambiranani izi:**

1. Kodi anthu adadziwa bwanji kuti Yohane anali m'neneri? (1:6)
2. Yohane adadza kudzachitanji?
3. Yohane adanena chiyani za Yesu? (1:7)
4. Yohane adawafunsa anthu chiyani asanawabatize? (1:4)
5. Kodi "kulapa" kutanthauza kutani?
6. "Akhristu akabatizidwa, amayenera kuyamba kuganiza za Mulungu, Yesu ndi Uthenga wabwino" Kodi izi ndi zowona kapena ayi?

## YOHANE ABATIZA YESU

Yesu anadza kuchokera ku Galileya nabatizidwa ndi Yohane mumtsinje wa Yordano (Mateyu 3:13). Yesu sadalape poti adalibe tchimo (Ahebri 4:15). Yohane anabatizaYesu popeza kunali koyenera kutero (Mateyu 3:15). Iyi inali nzeru ndi chikonzero cha Mulungu kuti ena akatengerepo phunziro la ubatizo. Yohane anadza kudzakonza njira ya ntchito ya Yesu, monga Mulungu adakonzera.




**Yohane abatiza Yesu mmadzi. (Mbalame ndi chizindikiro cha Mzimu Woyera.)**

Pamene Yesu adatuluka m'madzi, Yohane adaona zizindikiro zazikulu zitatu:

- Kumwamba kunatseguka.
- Mzimu woyera anatera pa Yesu.
- Mau anamveka kuchokera kumwamba ndi kuti: "Uyu ndi mwana wanga… mwa iyeyu ndikondwera".

Pambuyo pake Yohane adati: "Ndinaona Mzimu akutsika kuchokera kumwamba. Natera pa Yesu monga nkhunda. Ine sindinadziwa kuti Yesu kuti anali ndani, Koma Mulungu Atate wondituma kubatiza anthu ndi madzi adandiuza nati, "Udzaona Mzimu ukutsika kuchokera kumwamba Natera pa munthu, Munthu ameneyo adzabatiza anthu ndi Mzimu woyera". Ndipo ndinaonadi mzimu akutera pa Iye. Munthu uyu ndi mwana wa Mulungu. (Yohane 1:32-34)

**Kambiranani izi:**

1. Kodi Yohane adadziwa Yesu kuti anali ndani? (Yohane 1:32-34)
2. Ndichifukwa chiyani Yesu adamufunsa Yohane kuti amubatize iye?
3. Kodi mulungu atate adanena chiyani za mwana wake Yesu?
4. Ndi aneneri ati amene ananena za Mesiya (Khristu)? (Deteronomo 18:18; Yesaya 7:14)

**Mayina amene Marko adapatsa Yesu**

- Yesu Khristu (1:1)
- Mwana wa Mulungu (1:1 ndi 3:11)
- Yesu waku Nazareti (1:24)
- Woyera wa mulungu (1:24)
- Ambuye (1:3 ndiponso 7:28)
- Mwana wa munthu (2:28 ndi 8:31)
- Mbuye wa sabata (2:28)
- Mwana wa mkuiukulu(5:7)
- m'misiri wa mitengo (6:3)
- Mwanna wa Maria (6:3)
- Khristu (Mesiya) (8:29)

## Kuwerenga Baibulo: Marko 1:14-20

## UTHENGA WABWINO WOKAMBA ZA YESU

Yohane m'batizi anayitanira anthu ku kulapa ndikukhulupilira yesu Khristu-Mesiya. Timalapa pamene timva chisoni chifukwa cha machimo athu, ndikutembenuka kuleka kuchita machimowo. Yohane adauza mfumu Herodi kuti kunali kulakwa kuti iye atenge ndi kukwatira mkazi wa m'bale wake. Herodi adapsa mtima ndipo adayika Yohane m'myumba yandende kenaka adamupha. Koma Mulungu amadziwa zonse, Iye ndi wamphamvu zonse ndipo amalamulira zonse (Yesaya 46:9-10).

Kwazaka zambiri anthu achiyuda adakhara akuyembekezera Mesiya. Adafunafuna mtsogoleri amene akadatha kuwapulumutsa ku ulamuliro wa a Roma. Koma poyamba mulungu adafuna iwo atembenukire kwa iye ndi

kusiya njira zawo zoipa. Anthu ambiri olungama anali ataphedwa poyesayesa kupulumutsa ayudawa kumakhalidwe oyipa otengera kwa mitundu ina. Aneneri ambiri adaneneratu za wina amene adzabwere ndi kuwapulumutsa - Mesiya.

Lyeyu adzabwezeretsanso zonse zimene zidatayika, pamene Adamu adachimwa (Genesis 3:17-19; Deuteronomo 18:15; Yesaya 42:1; 49:6; Agalatiya 3:16) Munthu wolonjezedwayo anali Yesu. Yesu adanena kuti ufumu wa Mulungu wayandikira.

**Kambiranani izi:**

1. Kodi ndi uthenga wabwino wotani umene yesu adawauza anthu, (Marko 1:14, 15; Yohane 17:3)?
2. Kodi Satana adayesera chotani kulepheretsa nzeru ya Mulungu?
3. Ndi chifukwa chiyani anthu afunika kulapa? (Marko1:15)?
4. Kodi kulapa kutanthauza kutani?

## YESU AYITANA OPHUNZIRA AKE

Yesu anali kuyenda m'mbali mwa nyanja ya Galileya. Anaona Simoni ndi Andreya, m'bale wake alikuponya kombe mnyanja, (Marko 1:16) Yesu anawayitana nati "Idzani munditsate ine! " Lye adafuna kuwaphunzitsa iwo za ufumu wa Mulungu. Onani kuti Yesu anayitana anthu ogwira ntchito wamba kuti amutsate.




**Yesu aitana ophunzira ake oyamba kuti amutsate.**

Nthawi yomweyo anasiya usodzi wawo namutsatira Yesu. Lye adawalonjeza kuti adzawapanga ku khala asodzi awanthu osati nsomba. (Marko 1:17).

Andreya anali m'modzi mwa a kuphunzira a Yohane M'batizi. Anasiya kusata Yohane namutsatira yesu. Kenaka Andreya anapita kwa m'bale wake namuuza kuti, "Tamupeza Mesiya wolonjezedwa uja" (Yohane 1:40-41).

Ndipo Simoni anakhulupilira kuti Yesu Khristu ndi Mesiya ndipo adakhala m'modzi mwa ophunzira a Yesu. Pambuyo pake Yesu anati kwa Simoni "Dzina lako uzatchedwa Kefa". Ndilo losandulika Petro muchihelene kutanthauza

"thanthwe". (Yohane 1:42). Uyu ndiye Petro yemwe uja adamuphunzitsa Marko zonse adazidziwa za Yesu.

Tsopano Yesu anali wokonzeka kuphunzitsa akuphunzira ake, ndikuwauza anthu ena za ufumu wa Mulungu ndi kuyera kwake.

## Kuwerenga Baibulo: 1:21-28

## YESU AYAMBA KULALIKIRA NDI KUCHIRITSA

Yesu analowa m'Sunagogi (malo opempheleramo ayuda) ku Kapernao naphunzitsa anthu (Marko 1:21) Anthu anazizwa ndi chiphunzitso chake.

Musunagoge a Yuda anali kusonkhana ndi:

- Kupembedza ndi kupemphera kwa Mulungu; tsiku ndi tsiku;
- Kuwerenga ndi kuphinzitsa malembo achiheberi tsiku ndi tsiku;
- Kuchititsa sukulu ya a nyamata;
- Kukumana ndi akulu a chipembedzo otchedwa Alembi ndi Afarisi.
- Kuphunzira malamulo a Mulungu opelekedwa kupyorera kwa Mose
- Kumvetsera ziphunzitso, zimene wina aliyense wophunzira ndi wanzeru anali kuphunzitsa.

Atsogoleri awo anali kuwerenga chilamulo cha Mulungu tsiku lirilonse la sabata, koma Yesu analankhula za ufumu wa Mulungu ndi ulamuliro, (Marko 1:22). Munali mphamvu m'mau a Yesu ake ndipo anali kuphunzitsa kunena za ufumu wa Mulungu kuti yandikira. Mawu a Yesu anali amphamvu kwambiri kotero mizimu yoipa inali kufuula akamuona Iye. "Tili ndichiyani ife ndi inu Yesu waku Nazareti? Kodi mwaza kuzatiwononga ife?, Ndikudziwani, ndinu woyerayo wa Mulungu" (Marko 1:24).

Yesu anauza mzimuwo kuti, "Khala chete! " Tuluka mwa iye! Ndipo nthawi yomweyo Mzimu wa woipayo utuluka mwa munthuyo. Anthu onse anazizwa "Nati kuti Uyu ndani nanga Alamula mizimu yonyatsa ndipo imumvera iye? " anatero (Marko 1:27).

Taonani, Yesu sanafune kuti mizimu yonyansa ilankhule popeza inali kudziwa kuti iye anali ndani (1:25-34). Komabe posakhalitsa aliyense adadziwa za chiphunzitso cha Yesu ndi kutinso mizimu yonyasa inali kumvera iye. (Marko 1:27, 28).

### Kambiranani izi:

1. Yesu anali kufuna anthu ochenjera okha kuti akhale akuphunzira ake: Kodi izi ndi zowona kapena ayi?
2. Ndi chifukwa chiyani anthu anali ozizwa ndi chiphunzitso cha Yesu?
3. Kod mizimu yonyansa idamudziwa bwanji Yesu?

## Kuwerenga Baibulo: 1:29-45

## PETRO ATENGERA YESU KUNYUMBA

Kapernao unali mzinda umene unali cha kumpoto kwa nyanja ya Galileya. Yesu anakhalako kumeneko kunyumba kwa Simoni Petro. Apongozi a Simoni anali kudwala choncho Yesu anapita pafupi pawo nagwira dzanja lawo ndi kuwakhazika tsonga. Malungo awo anatheratu ndipo anayamba kuwatumikira iwo (1:31). Yesu anali ndi mphamvu ya kwa Mulungu yochita zodabwitsa. Anali kuchiritsa odwala. Popita dzuwa anthu ambiri anali unji unji pakhomo la nyumbayo (1:33) Anabwera ndi odwala ena wogwidwa ndi mizimu yonyansa. Yesu anawachiritsa onse. M'mawa wa tsiku lotsatira Simoni Petro anayitana anzake napita kofunafunaYesu.

Yesu anali ndi chizolowezi chodzuka kunja kusanache, ndikupita kumalo achete yekha kukapemphera (1:35) Anali kupemphera kwa Atate ake a kumwamba. Pemphero ndilo linali kumusunga mu mphamvu ndi chifuniro cha a Atate, Petro atamupeza Yesu anamuza kuti, "Anthu onse akufunafuna inu! Koma Yesu anayankha nati. Tiyeni tipite kumidzi ya pafupiyi, " Choncho adayenda kudutsa mbali ina ya galileya ndipo Yesu anali Kuyankhula m'misonkhano yawo. Analinso kutulutsa mizimu yoyipa ya ziwanda. (1:39)

## YESU ACHIRITSA MUNTHU WA KHATE

Munthu wina wodwala khate (nthenda ya Pa khungu) anadza kwa iye. Adagwada pansi namudandaulira Yesu kuti amuthandize. Anthu akhate anali kusiyidwa kunja kwa midzi ndi mizinda. Lye anati, "Ndidziwa kuti inu mungathe kundichiritsa ine ngati mufuna."

Yesu anamumvera chisoni ndipo anatambasura dzanja lake namukhuza nati, 'Ndifuna, khala wokozedwa.' nthawi yomweyo munthuyo anachiritsidwa. Yesu anamuuza kuti, "Pita ukadziwonetsere kwa akulu ansembe." Munthuyo anayenera kukadziwonetsera kwa akulu Ansembe ngati umboni woti wachiritsidwa. Pambuyo pake anali kuloledwa kubwelera kubanja lake. Anali kulumikizana ndi anthu ena onse osati kukhalanso pa yekha. Sanalinso Munthu wodetsedwa. Yesu adaletsa munthu wochiritsidwa uja kukawuza ena za amene anamuchiritsa. (1:44)

Koma munthuyo anali kuwuza aliyense amene anali kukumana naye. Posakhalitsa kunali kovuta kuti Yesu aziyenda yenda momasuka, chifukwa cha khamu la anthu (1:45).

**Kambiranani izi:**

1. Yesu atachiritsa munthu wodwala khate, ndi chifukwa chiyani adamuuza kuti asauze wina aliyense?
2. Munthu wochiritsidwayo anayenera kuti akadziwonetsere kwa ansembe chifukwa chiyani?
3. Mu bukhu la Marko, pezani pamene Yesu adapita kukapemphera m'mamawa.
4. Yesu anamuuza chiyani Simoni Petro (Yohane) (1:42)?
5. Ndi mnjira yotani imene ophunzira ake anati adzakhala asodzi a wanthu?

## Kuwerenga Baibulo: Marko 2:1-12

## YESU ACHIRITSA MUNTHU WOSATHA KUYENDA (WODWALA MANJENJE)


Yesu anapitanso kunyumba kwa Simoni Petro. Anthu ambiri atamva kuti ali kumeneko anadzadza nyumbayo kufikira kuti kunalibe malo (2:2). Yesu analalikira mawu a Mulungu. Mawu amulungu ndiwo uthenga wabwino wa chikondi cha Mulungu mwa Yesu Khristu (machitidwe 8:4).

Nyumba za ku Israel zinali kumangidwa ndi miyala yayikulu, zokhala ndi denga la thyathyathya la dothi, makande kapena dongo. Anthu anali kutha kuyenda pa dengapo. Nyumba zina zinali ndi madenga amatabwa kapena mapale. Amuna anayi anabwera ndi mzawo amene anali atadwalika wosatha kuyenda. Sanathe kulowa mnyumbamo chifukwa cha khamulo choncho adakwera dengalo nabowola tsindwi. Anamutsitsilapo wodwalayo amene anali gone pa kama wake kufikila pamapazi a yesu. Chikhulupiriro mwa Mulungu chimapangitsa anthu kuchita molimba mtima. Anthu okhala nacho chikhulupiliro amachita zinthu zazikulu chifukwa amadalira mwa Mulungu wamphamvu zonse. Yesu anawona chikhulupiriro chawo ndipo anati kwa odwalayo, "Mwana machimo ako akhululukidwa" (2:5).

(Uku kunali kuyankhura mwachifundo. Wodwalayo sanali mwana wa Yesu ayi).

Afalisi ndi alembi (aphunzitsi a chilamulo) anamumva Yesu ali kuphunzitsa; Iwo anafunsana nati; Ndani angakhululukire machimo a wanthu? Koma Mulungu yekha (2:7).

"Uyu achita mwano". Kuchitira Mulungu mwano (Masalimo 74:18; Yesaya



**Yesu ndi wolumala ali pa mphasa yake**

52:5; Aroma 2:24) linali tchimo lowopsya kwambiri m'masiku amenewa; Anthu wotero anali kuphedwa poponyedwa miyala (Levitiko 24:11-14).

Yesu anadziwa zimene iwo anali kuganiza, ndipo anawafunsa, "Chapafupi ndi chiti kunena kuti 'machimo ako akhululukidwa' kapena kuti 'nyamula mphasa yako nuyende? ' Ananena izi -kuti iwo adziwe kuti iye anali mwana wa Mulungu amene anali ndi mphamvu pa dziko yotha kukhululukira machimo ndi kuchiritsa" (2:9, 10).

Kenaka anamuchiritsa munthu uja. Anthu onse anawona munthuyo akudzuka ndi kumapita kwawo ndipo analemekeza Mulungu nanena, "Zotere sitinaziona ndi kale lonse" (2:12).

## Kuwerenga Baibulo: Marko 2:13-22

## YESU BWENZI LA OCHIMWA

Yesu anatuluka nalankhula ndi khamulo m'mbali mwa nyanja. Lye anafuna anthu asiye zawo zonse ndikumutsata iye. Tsiku limeneri anapeza Levi wakhometsa misonkho amene anali kutchedwanso kuti Mateyu. Amisonkho anali kugwirira ntchito boma la a Roma. Ndipo anthu sanali kuwakonda popeza analibe chilungamo. Anali kukhometsa anthu misonkho yandalama zochuluka. Ayuda anali kuwatchula ochimwa. Levi anasiya ntchito yake ya misonkho ndipo anamutsatira Yesu. (2:14)

Levi anamuyitanira Yesu ndipo ophunzira ena kukadya kunyumba kwake. Ayuda ena ndi aphunzitsi a chilamulo (Afarisi) anali pompo. Iwo anafunsana kuti "ndi chifukwa chiyani akudya ndi okhometsa misonkho amene ndi wochimwa? " Yesu anawauza kuti, 'Akulimba safuna sing'anga koma wodwala, sindinadze kudzayitana olungama' (2:17).

Yesu anafuna kuthandiza anthu omwe anali osowa kwenikweni. Anthu otere anali kumulandira Yesu koma atsogoleri achipembedzo sanali kufuna kuti amtsatire Yesu. Atsogoleriwa, monga ena onse anali kuyembekezera Mesiya koma sanafune Yesu.

## YESU AONETSERA NJIRA YABWINO YOCHITIRA ZINTHU

Afarisi anali kuganiza kuti iwo wokha anali anthu abwino. Anali kusala kudya ndiponso anali kuyesetsa kutsata malamulo a Mulungu. Mulungu anati anthu onse ali wochimwa. "Palibe m'modzi wakuchita bwino, n'nena m'modzi" (Masalimo 53:3).

Akuphunzira a Yohane anali kusala kudya. Anthu anali kusala pa zifukwa zambiri: -

- kuonetsa chisoni pamene wina wamwalira (Masalimo 53:3)
- kuti athe kuganiza mwakuya za mulungu ndi kutha kumupembedza (Nehemiya 1:4).

- kuti athe kusunga malamulo okhudza masiku oyikika ngati tsiku lakudzipatula la a Ayuda.
- Kuti akhale ndi nthawi yokwanira ya kupempherera china chake chofunika.

Yesu analankhula za phwando la ukwati wa chiyuda. Mkwati ndi mkwatibwi anali kutsekula makomo a nyumba yawo kuti alendo athe kulowa. Oyitanidwawo anali kufika ndi kudya mokondwa pamodzi ndi mkwati ndi mkwatibwi.

Lye anati umu ndi m'mene zidzakhalire pamene iye, monga mkwati anali pakati pa akuphunzira ake. Anati adzakhala nawo kwa kanthawi ndipo iwo adzakhala okondwa. Kenaka adzaphedwa ndipo iwo adzakhumudwa. Nthawi imeneyo ndi pamene ati adzasale kudya (2:20). Yesu anadza kudzawasonyeza njira yabwino koma kusakaniza zatsopano ndi zakale sikungathandize (2:21, 22). Lye anafuna anthu aleke njira zawo zakale ndi kumutsatira iye.

**Kambiranani izi:**

1. Kodi Yesu angathe kukhulukira machimo pambali pa Mulungu?
2. Kodi ndi chifukwa chiyani Yesu adati, "abwino safuna sing'anga? "
3. Ndi chifukwa chiyani atsogoleri a chi Yuda sanali okondwa kuona Yesu akudya ndi ochimwa?
4. Kodi ochimwa anadza kwa Yesu chifukwa chiyani?

## Kuwerenga Baibulo: Marko 2:23-28; 3:1-6

## YESU ACHIRITSA MUNTHU PA TSIKU LA SABATA

Afarisi anali okwiya ndipo Yesu anadziwa kuti anali kufuna kumupha iye (3:6). Anatsutsana naye za tsiku la sabata ndipo anafunafuna njira yoti amukole iye.

Yesu anachiritsa munthu amene anali ndi dzanja lopuwala pa tsiku la sabata. Yesu anadziwa zimene a Farisi anali kuganiza choncho anawafunsa "Lamulo limati tiyenera kutani pa tsiku la sabata? Kuchita zabwino kapena zoyipa? (3:4)

Pamenepo nkuti a Farisi atadzudzula akuphunzira a Yesu kuti sanayenera kuthyola ndi kudya ngala za tirigu pa tsiku la sabata (2:23-24).

Yesu anakwiya nawo a Farisi komanso anawamvera chisoni chifukwa mitima yawo inali yowuma (3:5). A Farisi sananene pa zinthu izi koma anangokonza chiwembu chofuna kumupha iye (3:6).

Yesu anachita chifundo kuchiritsa munthu wopuwala dzanja koma atsogoleri a chipembedzo anali owuma mitima.

Onani pa vesi 28 Yesu ananena za mwana wa munthu, anali kunena za iye mwini. Yesu ndi Mbuye wa onse (zonse).

# SABATA

Sabata litanthauza kupuma, Kuleka kugwira ntchito. Mulungu anawuza Adamu za m'mene iye adakonzera kumwamba ndi dziko la pansi mmatsiku asanu ndi limodzi ogwira ntchito pa tsiku la chisanu ndi chiwiri Mulungu adapuma osagwira ntchito yake. Adalitchura tsiku la chisanu ndi chiwiri sabata (Genesisi 2:3).

Kenaka, Mulungu adapereka malamulo ake kwa Mose. Mu malamulo a Mulunguwa sabata linayeretsedwa (Ekisodo 20:8-11). Patsiku la sabata amuna ndi akazi adapuma kuntchito zawo napembedza Mulengi wawo. Sabata linali tsiku lotsiliza kapena kuti la chisanu ndi chiwiri la pa Mulugu. Linali kuyamba polowa pa dzuwa pa tsiku la chisanu. Zachisoni kuti a Farisi adawonjezera malamulo awo pa malamulo a sabata. Adaganiza za kusunga sabata kwambiri kuposa za kupembedza Mulungu. Akhristu oyambirira pachiyambi anali kukumana ndi kupembedza pa tsiku la sabata.

Kenaka anayamba kukumana ndi kupembedza pa tsiku loyamba la pa Mulungu tsiku la mulungu. Tsiku la mulungu linasanduka tsiku lopuma ndikupembedza kwa akhristu ambiri. Okhulupilira ena amasungabe sabata la tsiku la chisanu ndichiwiri monga Ayuda.

Kodi Yesu sangathe kukhala Mbuye wa tsiku lirilonse? Inutu mungathe kupembedza pa tsiku lirilonse, ndipo tsiku lirilonse lidzakhala Sabata kwa inu! Tsiku lirilonse lidzakhala tsiku lopuma mwa Mulungu kwa inu, ngakhale mukugwira ntchito zanu.

## Kuwerenga Baibulo: Marko 3:7-19

# YESU ASANKHA AMUNA KHUMI NDI AWIRI

Yesu anapita pa nyumba ina yapafupi ndi nyanja. Anthu ambiri adadza kudzamvera iye. Anthu anali kumukankha ndi kumutsamira choncho iye adalowa mu bwato nawaphunzitsa iwo ali pamadzi, Potsatira iye anakwera kupita ku mapiri. M'mawa mwa tsiku lotsatira, iye anayitana otsatira ake ndi kusankhapo khumi ndi awiri kukhala ophunzira ake:

- Kuti adzikhala ndi iye
- Kuti awaphunzitse iwo
- Kuti awatume kukalalikira
- Kuti awapatse iwo mphamvu yochiritsa ndi yotulutsa ziwanda (3:15).

Kwa zaka zitatu, Yesu adaphunzitsa khumi ndi awiriwo kukhala atumiki a Mulungu.

**Kambiranani izi:**

1. Kodi ndi kulakwa kutola ngala pa sabata?
2. Ndi chifukwa chiyani anthu anali kusala?
3. Patsiku la sabata tiyenera kuchita zotani?

4. Yesu anatanthauzanji pamene anati, " Tsiku la sabata linapangidwa chifukwa cha munthu" (2:27)?
5. Panali kusiyana kotani pakati paziphunzitso za Yesu ndi ziphunzitso za atsogoreri a mipingo? "
6. Anthu angaphunzire bwanji kukhala otumikira a Mulungu?

## Kuwerenga Baibulo: Marko 3:20-35

## MPHAMVU YA MULUNGU ILI YOPOSA YA SATANA

Yesu anali kutulutsa ziwanda mwa anthu (1:39) ndipo afarisi anakamba za izi. lwo anati iye atulutsa ziwanda ndi mphamvu ya mfumu ya ziwanda (satana) (3:22). Yesu anawafunsa kuti, 'Kodi satana angapilikitse satana? Iwo sanathe kumvetsa ndipo Yesu anagwiritsa ntchito zifanizo zitatu izi:

- Ufumu wa anthu amene akungomenyana okhaokha
- Nyumba kapena banja la anthu amene akungokangana ndi kumenyana pakati pa wo.
- Satana angathe bwanji kumenyana ndi Satana?

Pali maufumu amizimu awiri padziko. Ufumu wa Mulungu wa chikondi ndi kuwala ndi ufumu wa satana wa mdima ndi zoyipa. Mizimu yonyansa ya satana imadana ndi chilungamo ndipo imalimbana ndi atumiki a Mulungu. Ichi ndi chifukwa chake Yesu adaphunzitsa akuphunzira ake kuti popemphera aziti: "Mutipulumutse ife kwa woyipayo" (Mateyu 6:13).

Mu ufumu wa Mulungu choyipa chimagonjetsedwa ndipo machimo amakhululukidwa (3:28). Koma palibe m'modzi amene angakhululukidwe, ngati anenera mzimu woyera wa Mulungu mwano (3:29).

Satana akuyelekezedwa ndi munthu wamphamvu amene Yesu anali kumunena mu mwambi uja (3:27). Munthuyo amamanga anthu m'machimo awo.Yesu adadza kuti amange munthu wamphamvuyo ndi kumasula iwo osungidwa mu ndende zake. Yesu anadza kudzamasula anthu ku machimo awo (Agalatiya 3:22). Adadza iye kudzamasula anthu kumalamulo opangidwa (Agalatiya 3:23).

## YESU NDI AMAYI AKE NDI ABALE AKE

Poyamba kuwerenga nkhaniyi, tiwona ngati kuti Yesu sanali kufuna kuona amayi ndi abale ake. Pa vesi 21 zikuwonekeratu kuti anali atabwera kudzamutenga. Iwo anali ndi nkhawa chifukwa cha zonena za anthu kumudzi kwawo ku Nazareti. Abale ndi a bwenzi awo anali kuganiza kuti Yesu anali wozerezeka (wopenga).

Choncho Yesu anakana kuwonana nawo kuopa kuti angalepheretse chifuniro cha Mulungu. Yesu anakhala ndi anthu amene anali kuthandizira chifuniro cha Mulungu pa iye. Khamu lomwe limafuna kuwonana ndi iye kuti

ali phunzitse ndi kulichiritsa. Aliyense amene amvera Mulungu ndiwo mayi wanga, ndi abale anga (3:35)

Apa sindiye kuti Yesu anakana amayi ndi abale ake. Akadatulukabe panja kuonana nawo. Anachita chimene chinali choyenera ndi cha ulemu kwa abale ake. Nthawi zina anansi ndi azibale anthu akhoza kutijejemetsa kuchita chifuniro cha Mulungu. Tiyenera kuwalemekeza, komabe tiyenera kudaiira kwa Mulungu ndi kuchita chifuniro cha iye popanda kudana ndi abale anthu.

**Kambiranani izi:**

1. Kodi Yesu adaonetsa bwanji chikondi chake kwa amayi ndi abale ake?
2. Tikakhala ndi zopyinja za pa ubale, tiyenera kuganizira za yani poyambilira?
3. Otsatira a Yesu ali mbali ya banja lalikulu la padziko lonse (Marko 3:34; 35). Kodi izi zitanthauzanji kwa anthu okhala pa dziko?

## MAFANIZO

Yesu anagwiritsa ntchito mafanizo, kuphunzitsa choonadi kwa womutsatira. Fanizo ndi nthano ya zochitika tsiku ndi tsiku koma yokhala ndi tanthauzo lauzimu lakuya. Lye anali kumasulira fanizolo pambuyo pake kwa ophunzira ake (4:13). Analipo ena mu gululo amene sanafune kumva zowona. Iwo sanafune kumvetsetsa (4:24-25). Amene sanafune kudziwa choonadi cha Mulungu anayesetsa kumva tanthauzo la nthanozo. Mzimu wa Mulungu amavumbulutsa zambiri za choonadi m'mitima ya iwo ofuna kumudziwa Mulungu (Mateyu 13:14-15).

## Kuwerenga Baibulo: Marko 4:1-25

## FANIZO LA WOFESA

Yesu analowa mungalawa nayambanso kuphunzitsa anthu. Mawu ake anamveka kutali popeza kunali bata. Mu fanizoli, mlimi ofetsa mbeu ali ngati munthu wonena za uthenga wabwino. Mbeu ikuyimira choonadi cha uthenga wa Mulungu – uthenga wa bwino. Wofetsayu akubzyala mu dziko. Lyeyu ndi mboni. Mboni ndi amene amanena zimene adziwa kapena zimene wawona. Wofetsayo ananyamula mbewu muthumba. Anali kumwaza mbewu kulikonse kumene anali kufikira (4:4).



Fanizo la wofesa

Mawu a Yesu anali ngati mbewu imeneyi. Mitima imene inali yotseguka inatha kulandira choonadichi ngati m'mene nthaka yabwino inali yakutha kulandira mbeu. Mitima youma sinali yokhoza kulandira choonachi.

Pambuyo pake Yesu anamasulira fanizoli kwa akuphunzira ake:

1. Mitima ina ndi yowuma ngati nthaka ya m'mbali mwa njira. Mitima yotere siingathe kulandira uthenga wa bwino wa Yesu khristu. Dothi lake ndilolimba kotero mbewu siingamere.
2. Nthaka ya pathanthwe ikuyimira mitima imene imatha kulandira mwansanga uthenga Wa Mulungu koma yosachedwa kutaya chikhulupiliro mavuto akabwera. Mbewu imamera msanga m'mithuzi ya mathanthwewo, koma dothi lake ndi lochepa moti mbewu singazikike ayi. Dzuwa likatentha ' mbeu zimanyala ndi kufa.
3. Mbewu yogwera pakati pa minga ikuyimira moyo odzadzidwa ndi zinthu zina. Adani atatu amoyo amene amatsamwitsa ndi kuwononga mbewu akuperekedwa (Mateyu 19:22)
   - Chikondi cha pandalama
   - Kufunafuna zinthu zochuluka za dziko la pansi.
   - Kufunafuna chisangalalo ndi kupambana (1 Yohane 2:16).
4. Mbewu yogwera pa nthaka yabwino ili ngati choonadi chimene mtima wotseguka umachilandira. Nthakayo ndi ya bwino ndiponso yakuya ndi yokonzedwa bwino. Mbewu imera nibala zipatso zambiri. Zipatso zikuyimira chikhulupiliro chenicheni ndi ntchito zabwino zimene zimatsatira.

Timafetsa mbewu pamene tiwuza ena za choonadi cha Mulungu ngakhalenso pamene tiwapatsa Baibulo kuti awerenge. Anthu ena safuna kumvera. Ena amamva koma osamvetsetsa. Enanso amafulumira kumtsata Yesu komansos amakhumudwa msanga. Awa amagwetsedwa mphwayi chifukwa cha chikhulupiliro chofooka. Komanso ena amatsatira njira yatsopano ya Yesu kenaka ndi kutayika chifukwa chofuna kuyesayesa zina za tsopano.

Yesu anawachenjeza anthuwo kuti ngati satha kumvetsa fanizoli sangathenso kulandira tathauzo lako (Marko 4:13). Koma iwo akumva ndikuzindikira zinthu izi, adzakhala moyo waphindu mu ufumu wa Mulungu (4:20). Fanizoli likuwonetsa kusiyana pakati pa anthu opulumutsidwa ndi anthu otayika. Zikutiwonetsera zimene zimachika kwa anthu amene samvetsera bwino choona cha Mulungu. Anthu ambiri samvetsa zinthu izi.

Yesu ali ngati nyali. Ayenera kukwezedwa kuti anthu onse awone kuwala ndi chilungamo cha Mulungu (Marko 4:22; Yohane 1:4, 5). Pamene anthu afika ku kuwalaku, Mzimu woyera amawapatsa kuwala kowonjezera. Mulugnu amapereka kuwala mu nzeru zawo ngati amvetsera ndi kukhulupirira.

**Kambiranani izi:**

1. Kodi m'neneri Yesaya ananena chiyani za mitima yowuma? (Marko 4:12)
2. Kodi nthaka yabwino ndi chiyani?
3. Tingathandize bwanji kuti mbewu imere m'mitima ya ena?

## Kuwerenga Baibulo: Marko 4:26-39

## MAFANIZO A CHIKHULUPILIRO NDI UFUMU WA MULUNGU


Yesu analankhula za chyembekezo ndipo popanda chikhulupiliro munthu sangathe kumkondweletsa Mulungu. Ophunzira a Yesu sanamvetse zimene iye anali kunena za ufumu wa Mulungu. Yesu anagwiritsa ntchito zitsanzo za moyo wa tsiku ndi tsiku. Munthu wofetsa mbewu anayenera kukhala nacho chiyembekezo:

- Ayenera kugwiritsa ntchito mbewu yabwino imene akukhulupilira kuti imera.
- Ayenera kudikira modekha kuti mbewu imere.
- Ayenera kukhulupilira kuti mbewu izatha kumera.
- Ayenera kukhulupilira kuti idzabala zipatso zochuluka zodzakolola (4:29).

Yesu ananenanso fanizo la ufumu wa Mulungu. Kunena kuti, Ufumu wa Mulungu uli ngati kambewu kampiru kochepa. Chaka chisanathe kakula kuposa mbewu zina zonse, mwina kufikira mapazi khumi ndi awiri kapena mamita anayi. Ufumu wa Mulungu padziko udayamba mochepa. Otsatira a Yesu sanali anthu odziwika. Iwo anali anthu wamba opanda mphamvu. Koma anatha kufalitsa ufumuwu ku maiko ambiri (Machitidwe 1:8; 17:6). Lero choonadi ichi chikulalikidwa pena paliponse ndipo amuna ndi akazi ali ndi ufulu kukana chilungamo cha Mulungu kapena kukhulupilira ndi kupulumutsidwa polumikizana ndi mpingo wa chikhristu.

## AKUPHUNZIRA AWOLOKA NYANJA

Yesu anawauza akuphunzira kuti awolokere kutsidya lina la nyanja. Pamene anali kuwoloka, namondwe anayamba ndipo mafunde anayamba pa nyanjapo. Bwato limene anakwera linali lochepa ndipo wophunzirawa anachita mantha. Yesu analibe mantha, Iye anali kugona. Ndipo anamuzutsa nati, "Mphunzitsi kodi simusamala kuti titayika ife? " Akuphunzira anafunsa Yesu (4:38). Yesu anawuka nati tonthola, khala bata! ndipo mphepo inaleka ndipo panyanja panali bata.



Yesu aletsa namondwe

Ndipo iwo anayang'anana wina ndi m'nzake. Mmodzi wa iwo anafunsa nati "Uyu ndani? Kuti mphepo ndi mafunde zimvera iye" (4:41). Tsopano anachita mantha osati pamafunde koma anaopa Yesu. Anali oposa munthu anali Mulungu. Yesu anafuna kudziwa chifukwa chimene iwo sanathe kudalira pa iye kuwateteza. Pamene mitima yathu ikhala ngati nyanja ndipo sipeza mpumulo Yesu amanena chimodzimodzi kwa ife "Khala chete! Ndiri ndi iwe. Dalira ine."

**Kambiranani izi:**

1. Kodi ufumu wa mulungu udalitsa bwanji mitundu?
2. Ufumuwu umakula bwanji?
3. Kodi mbewu ya mpiru itiphunzitsa chiyani za ufumu wa Mulungu?
4. Tingatani kuti tithandizire ufumuwu kukula?

## Kuwerenga Baibulo: Marko 5:1-20

## YESU AMABWERETSA MTENDERE M'MITIMA YA WANTHU



Yesu achiritsa munthu wa ziwanda zambiri

M'mbali mwa nyanja munalinso manda, mapanga amene anthu anali kuyikamo akufa awo. Munthu waziwanda anali kukhala kumeneko (5:3). Mizimu yonyansa inamupangitsa iye kukhala wa mphamvu ndi wa ukali. Anthu anayesa kumumanga ndi maunyolo koma anali kudula ndi kuthawa. Munthuyu atamuwona Yesu akutsika mu bwato

anamuthamangira ndi kugwa pamawondo ake (5:6).

Ziwanda zinadziwa kuti Yesu anali ndani. "Ndiri ndi chiyani ine ndi inu, Yesu mwana wa Mulungu wa mkulukulu? Ndikulumbilirani pa Mulungu musandizunze! " (5:7) Ziwanda zinamudziwa ndikumuwopa Yesu. Ziwanda zimadziwa kuti Yesu ndi mwana wa Mulungu. Zimadziwa kuti iye ali nawo ulamuliro pa izo ndipo zimamuwopa iye. (Yokobo 2:19).

Zimadziwa kuti Yesu ndi mbuye wa chilengedwe. Akalamula ziwanda ndi mizimu yonyansa, zimamvera iye.

Marko akusonyeza kuti Yesu ali ndi mphamvu pa zinthu zonse. Lye analora kuti ziwanda zipite mu gulu la nkhumba (aYuda sadya nkhumba) Munthuyo anawona nkhumba zikuthamanga ndi kulowa pa nyanja ndipo anadziwa kuti wamasulidwa. Lye anamasulidwa ku mizimu yonyansa. Anali nacho chikhulupiliro mwa Yesu ndipo anayamika Mulungu. Amene anali kuweta nkhumbazo anathawanso. Iwo anabwelera kumudzi kukawauza eni nkhumbazo zazimene zidachitika. Anthu atamva anabwera kuti adzadziwonere okha (5:14).

Anapeza kuti munthuyo anali atachira ndipo anali khale pa mapazi aYesu. Anthu a m'mudzimo anaopa. Poyamba anali kuchita mantha ndi wa ziwanda. Koma tsopano anayamba kuwopa mphamvu ya Mulungu (5:17). Nkhumba zawo zinasowa, choncho iwo adapempha Yesu kuti achoke m'dela lawolo.

## MUKA KWANU, UKAWAUZE ABALE AKO”

Munthuyo anali atayima pa mbali pa Yesu pa gome. Analibe abwenzi, analibe chakudya, analibe ntchito ngakhalenso malo okhalako. "Lolani ndi muke nanu inu", anamufunsa Yesu. Yesu ananena naye, "Muka kwanu kwa abale ako ndipo ukawauze zinthu zadzikulu anakuchitira Ambuye" (5:19). Kwa zaka zambiri satana anadzetsa umphawi pa banja la Munthuyu. Iwo anasowa mwana wawo, bambo kapenanso mwamuna. Tsopano inali nthawi yakuti abwerere kwa abale ake ndi kuwawuzanso ena zimene Yesu anamuchitira iye ndi kuwuzanso ena za Yesu.

Nthawi zambiri, Ufiti kapena chigololo, kapena mankhwala osokoneza bongo, kapena zoledzeletsa, kapena njuga zakhala zikuwononga ziwalo za mabanja. Makolo okhala ndi nkhanza. Pochita zinthu izi timayitanira ziwanda m'moyo wathu. Ndi Yesu yekha amene angathe kutulutsa ziwanda. Ndi Yesu yekha amene angawapatse okondedwa anthu mzimu wa mphamvu, ndi chikonndi ndi kudziretsa. (2 Timoteo 1:7)

**Kambiranani izi:**

1. Ndichiyani chingamupangitse munthu wa ziwanda kukakumana ndi Yesu?
2. Yesu adazifunsiranji ziwandazo dzina lawo?
3. Kodi mizimu yonyansa imamudziwa Mulungu?
4. Ndi chiyani chidawoneka kwa nkhumba zija?
5. Anthu m'mudzi muja anaonanji atafika kumanda?
6. Munthuyo adapita kuti kumene adakawauza anthu za Yesu?

**Ophunzira khumi ndi awiri a Yesu**

**Simoni:** Wochokera ku Betisaida, msodzi wa nsomba.Yesu adamupatsa dzina loti Petro (thanthwe)

**Yakobo:** Mwana wa Zebedayo, wotchedwa Yakobo wamkulu m'bale wake wa Yakobo, ndi **Yohane:** m'bale wake wa Yakobo.

**Andreya:** M'bale wa Petro (Yohane 1:40).

**Filipo:** Amene adapita ndi kukapeza natanielo.

**Natanielo:** Amenenso anatchedwa Bartimeyo (Yohane 1:43).

**Tomasi:** (Yohane 1:16; 14:5).

**Yakobo:** Mwana wa Alufeyo wotchedwanso Yakobo wa mng'ono (Marko 15:40).

**Mateyu:** Wa misonkho (Levi Mateyu 10:2).

**Tadeyo**: Wodziwikanso ndikuti Yuda.

**Simoni:** Wotchedwa Zeloti (Luka 6:15).

**Yudase Iskariote:** Wochokera ku Kariote amenenso anampereka Yesu.

## Kuwerenga Baibulo: Marko 5:21-43

## ZA MAYI WA NTHENDA YACHIDWALIRE NDI MTSIKANA WAKUFA

Yairo, m'modzi wa akulu wasunagogi anadza kwa Yesu ndi kugwada nati: "Kamwana kanga ka buthu kali kutsilizika, Ndikupemphani inu mufikeko, muyike manja anu pa iko" (5:23). Khamu lalikulu linali kumukanikiza iye.


Ndipo munthu wamkazi wachidwalire anadza pafupi ndi iye. Anali atamwaza ndalama zambiri kugulira mankhwala, koma osachira. Mwachikhulupiliro anasendera pafupi ndi Yesu nakhudza mphonje ya chovala cha Yesu. Nthawi yomweyo anachiritsidwa. Mulungu nthawi zonse amayankha chikhulupiliro chathu chochepa. Yesu anacheuka ndi kufunsa, "Ndani wandikhudza ine"? Anali atazindikira kuti mphamvu zake zina zachoka mwa iye (5:30; Luka 8:45). Mpamvuzo sizinali

muzovala zake ayi. Mphamvu inali mwa Yesu, mu umunthu wake. Mayiyo adazindikira kuti adachiritsidwa (5:29).

Anagwa pamapazi a Yesu. Yesu anamuuza kuti, "Chikhulupiliro chako chakuchiritsa, muka mumtendere, nukhale wochira mukuvutika kwako" (5:34).

Palibenso amene adalankhulapo mawu ngati amenewa kwa mayiyo chiyambire. Mwinatu inuyo mungakhale ndi nthenda kapena wina adakukhumudwitsani ndipo munamva kuwawa, ndikutheka kuti kuwawako ndi kwa kale, ndipo zikuvuta kuti muyiwale. Fikani kwa Yesu. Lye akudikirira kuti mumulandire ndikumukhulupilira, ndipo adzathetsa zowawazo.

Yailo anali kudikirabe Yesu. Amithenga adadza kwa iye ndi uthenga woyipa. Iwo anati mwana wako wafa; uvutiranjinso mphunzitsi? Usachite mantha, tangokhulupirira (Marko 5:35-36). Koma Yesu anasankha Petro, Yakobo, Ndi Yohane m'bale wa Yakobo kutsagana naye m'nyumba. Lye anali kukonda kukhala pafupi ndi atatu amenewa (Marko 9:2).


Yesu aukitsa kamtsikana kwa akufa

Iwo adakumana ndi wokhuza maliro akukuwa kwambiri. "Mwanayo sanafe koma akugona", Yesu adawauza. Iwo adamuseka iye pwetepwete (5:40).

Yesu anagwira dzanja la mtsikanayo ndikunena, "buthu, ndinena ndi iwe, uka! " Nthawi yomweyo mzimu wamtsikanayo udabwerera mthupi lake. Anadzuka nayamba kuyendayenda.

Yesu ali ndi mphamvu yotha kuchiritsa anthu ndi kuwabwezera moyo. Mukhudzeni iye mwachikhulupiliiro. Dikirani pa iye mwa pemphero kulinga kuzosowa zanu zonse. Lye adalonjeza kuti adzayankha zonse (Aheberi 13:8; 1 Petro 5:7).

## 🕮 Kuwerenga Baibulo: Marko 6:1-13

## ANTHU AMUKANA YESU

Yesu anabwereranso ku Nazareti kumene iye adakulirako (Marko 1:9; Luka 2:39). Lye adaphunzitsa mu Sinagoge nyumba ya aYuda yopempherelamo, pa tsiku la sabata. Ambiri amene adamumva iye anazizwa (6:3). Koma iwo sanakhulupilire kuti iye anali Mesiya kapena kuti khristu. Iwo adamudziwa ngati mwana wa wosema matabwa (6:2). Ndiponso kumeneko anangochiritsa anthu wochepa okha. Anthuwo sanathe kumukhulupilira. Iwo anakhulupilira kuti

Yesu anali mwana wa Yosefe ndi Mariya. Iwo sanakhulupilire kuti Yesu anali mwana wa Mulungu.

## YESU ATUMA AKUPHUNZIRA

Yesu anachoka ku Nazareti napita ku midzi ina ya mu Galileya. Nthawi yake yokhala pa dziko inali itasala pang'ono kutha, koma malo ambiri anali asanamve za uthenga wa bwino. Lye anatuma aku phunzira ake kumalo enawo. Yesu anawapatsa akuphunzirawo mphamvu pa mizimu yoyipa ndipo anali ndi mphamvu yake yochiritsa matenda (6:7).

Onaninso kuti iye anawauza iwo kuti" Musatenge mkate, thumba kapena ndalama mchiuno mwanu. Iwo anali kupita kukagwira ntchito ya Mulungu choncho sanafunikira kudera mkhawa za chakudya kapena ndalama (4:19; 6:8). Iwo anayenera kudalira pa Mulungu basi.

Mphamvu imene inali mwa akuphinzira ili ndi ife. Akuphunzira anapita kukaphunzitsa kuti anthu alape ndikuleka machimo awo ndiponso kuti abwere kwa Mulungu (6:12). Onani kuti iwo sanapite okha, koma anayenda awiri awiri (6:7).

Banja lililonse likawalandira anali kulowa mnyumba ndi kuwaphunzitsa za Mulungu. Anali kutulutsa ziwanda ndikutsanulira mafuta pa wodwala ndipo anali kuchira (6:13).

**Kambiranani izi:**

1. Kodi ndi ndani adakhulupilira Yesu, Yairo kapena mwana wake wa mkazi?
2. Kodi mayi adakhudza Yesu uja, adakhulupilira Yesu kapena chovala cha Yesu?
3. Ndi chifukwa chani Yesu sanachite zozizwa za mbiri ku Nazareti?
4. Kodi liu loti kulapa litanthauzanji?

## Kuwerenga Baibulo: Marko 6:14-44

## HERODE APHA YOHANE M'BATIZI

Mfumu Herode analamulira mu Galileya. Lye sanali bwenzi la a Yuda koma a Roma, lye anali kutchedwa 'Mfumu' chifukwa anali woyang'anira dera lalikulu la Israel (Mateyu 14:1) iye anamva kuti Yesu anali kuchiritsa anthu odwala ndikuti anali kutulutsa ziwanda. Anthu ena anali kunena kuti "Mulungu wawutsa Yohane mbatizi kwa akufa". Ena anali kuti, 'lye ndi Eliya'.

Herod izi adavutika nazo m'mtima chifukwa cha tchimo lake, lye adayika Yohane Mbatizi mndende chifukwa chomdzudzura (6:16-18). Yohane adati kwa Herode, 'sikuli kwa bwino kuti iwe utenge ndi kukwatira mkazi wa m'bale wako Filipo'. Herodiya mkazi wa Herode anamuda Yohane ndipo adapangitsa kuti mwamuna wake amupemphe, potsata lonjezo limene Herode adalonjeza Salome, mwana wa Herodiya. Herode sadathe kunena kuti lonjezo lake linali

lolakwika popeza panali alendo wofunikira, ndipo sanafune kuganiziranso za izi (6:27).

Mwina Herode adafuna kudzamumvanso Yohane kapena kumuwona Yesu. Nthawi ina, Yesu Adangoti chete osamuyankha Herode pamene adamutengera kwa iye pomuyimba mlandu (Luka 23:9). Yesu adadziwa kuti munthu woyipayu sanali wokhoza kulepheretsa chikonzero cha Mulugu, chakupulumutsa anthu ku machimo awo.

## YESU ADYETSA ANTHU ZIKWI ZISANU


Yesu ndi akuphunzira ake sanathe kudya popeza anthu ambiri anali kubwera ndi kupita (6:31). "Tiyeni kumalo achete". Lye anawawuza akuphunzira. Choncho anakwera bwato nawolokera kutsidya la nyanja ku Betisayida (Luka 9:10). Anthu adamuwona Yesu akuchoka choncho iwo adathamanga natsogola. Ena ananyamula wodwala kuti akamupeze nawo. Yesu anawamvera chisoni chifukwa anali ngati nkhosa zopanda m'busa.

Anawona nkhawa ndi kusowa kwawo ndipo anayamba kuwaphunzitsa. Koma akuphunzira ake anali atatopa ndipo anafuna Yesu kuti awatumize anthu aja kumidzi ya kwawo chifukwa:

- Kumene analiko kunali kutali ndi malo odyera kapena kuti angagone.
- Kunja kunali kutada.
- Anthuwo anali ndi njala.

Yesu adawawuza akuphunzira ake kuti, "apatseni chakudya kuti adye". Fillipo, m'modzi wa akuphunzira anati, "Malipiro a miyezi isanu ndi itatu sagathe kugula chakudya chodyetsa anthu awa" (Yohane 6:7). Andreya anati "Pali m'nyamata ali ndi nsomba ziwiri ndi mikate isanu komabe izi zingadyetse khamu limeneri?" (Yohane 6:8). Yesu anawauza anthu kuti akhale pansi. Lye anayamika Mulungu nanyema mikateyo. Anapereka kwa akuphunzira ake amene anapatsa anthu (Marko 6:41).

Akuphunzira anazizwa. Mkate sunali kutha m'manja mwawo ngakhale anali kugawa. "Anthu onse anadya ndipo anakhuta. Onani kuti Yesu anagwiritsa ntchito akuphunzira ake kuchita chozizwitsachi. Kawirikawiri akhristu amadandaula kuti ntchito yakula koma Mulungu watipatsa zonse zimene tingagwiritse ntchito ndiponso kupyolera apo."




**Yesu adyetsa anthu 5000**

Mulungu mokondwera amagwiritsa ntchito zomwe tilinazo, koma ife tikachita dyera, sitingathe kuona zodabwitsa zikuchitika ndizopereka zathu.

**Kambiranani izi:**

1. Chifukwa chiyani khamu lonse lija linadetsa nkhawa akuphunzira a Yesu?
2. Kodi tiyenera kutani ngati ntchito ya Mulungu yatikulira ife?
3. Chikhulululupiliro chathu chingakule bwanji?

## Kuwerenga Baibulo: Marko 6:45-56

## YESU AYENDA PA MADZI

Yesu adawatuma akuphunzira amuke pa bwato ndipo iye anabalalitsa khamu la anthu lija. Lye anakwera paphiri kukapemphera. Yesu anawona akuphunzira kupalasa bwato lija ndipo adawatsata akuyenda pa madzi. Akuphunzira anamuwona iye akuyenda pamadzi ndipo anakuwa mwamantha. Kenaka anamva mawu, "Limbani mtima; ndinetu, musaope" (6:50). Anawadziwa bwino mawu a Yesu ndipo anazindikira kuti sanali mzukwa. Mantha onse anatha atamva mawu ake amene adawapatsa mtendere. Lye anakwera nalowa kwa iwo m'ngalawa ndipo mphepo inaleka (6:51).

Izi ziri ngati 'mphepo' zimene zimawomba pa moyo wathu. Ife timavutika ndi kulimbana ndi ntchito chifukwa timakhala nawo mantha ndipo sitidalira pa Mulungu. Kenaka Yesu amadza kwa ife ndipo mantha athu amachoka. Yesu amabweretsa mtendere ndi kulimbika mwa ife. Mavuto athu amasanduka ochepa pamene iye ali ndi ife, mwa chikhulupiriro. Tawonani akuphunzira analibe chikhulupiriro chokwanira. Anamutsatira Yesu ndi kuwona Mulungu akugwira ncthito, komabe anadabwa m'mene, iye anatontholetsa Nyanja ndi kuyenda pamadzi. Yesu ndi akuphunzira ake atangofika ku Genesarete, nakacheza pa doko, anthu ambiri anathamangira kwa iye atanyamula wodwala pa mphasa (6:53-55).

**Kambiranani izi:**

1. Kodi akuphunzira anaganiza bwanji pamene Yesu adawatsogoza mungalawa?
2. Ndichifukwa chiyani Yesu anapemphera usiku umene uja m'malo mongogona?
3. Akuphunzira anafuna ufumu wa dziko lapansi, zowona kapena zonama?
4. Potsiliza chaputala cha chisanu ndi chimodzi akuphunzira anadziwapo chiyani za cholinga cha Yesu, ndi chisamaliro chake cha anthu ndiponso mphamvu yake.

## Kuwerenga Baibulo: Marko 7:1-37

## CHIPHUNZITSO CHA AFARISI

Ayuda opembedza anali kukonda kusamba m'manja asanadye chakudya. Amasamba mwakatimwakati malinga ndi mwambo wawo. Iwo sanali kudya kanthu osasamba m'manja. Kutero kunali kulakwira chikhulupiriro chawo monga afarisi.

Yesu anawatcha afarisiwa 'onyenga'. Ena a iwo sanali kutsata zimene iwo amaphunzitsa anthu ena kuti azitsata. Iwo anali kungosonyeza kuti ali woyera posamba manja awo osati kutsuka mitima yawo. "Chochoka kunja sichingathe kudetsa munthu" (7:15). Mulungu amawona mumtima wa munthu. Lye amadziwa chimene ife tiliri ndi m'mene tiriri mkati mwathu.

Yesu anawauza afarisi kuti, "Yesaya ananena zowona za inu, " (Yesaya 29:13). M'neneriyu ananena uthenga wa Mulungu kwa atsogoleri a Chiyuda wonyenga. Mawu a mneneri anayenera kuwapatsa maganizo, koma afarisi wonyengawa anakana kumva mawu a Mulunngu nakakamirabe pa miyambo yawo. Afarisi anakondabe kuchita zimene makolo awo adawaphunzitsa kusunga. Kusamba m'manja asanadye chinali chimodzi mwa zizolowezi zawo.

Yesu anawauza kuti anali kusintha malamulo a Mulungu. Lye anawapatsa chitsanzo chakuti sanali kumvera lamulo lakuti 'lemekeza atate wako ndi amayi ako'. Iwo anayika lamulo lawo m'malo mwake. Anali kulora mwana kuleka kuthandiza makolo ake ponena kuti "Korbani". Korbani unayimira mtulo kwa Mulungu, ndipo kawirikawiri zinali ndalama. Potero anthu anali kukana kuthandiza makolo awo pazosowa.

Pambuyo pake akuphunzira adamfunsa iye za fanizo la zinthu zomudetsa munthu. "Kodi simutha kumvetsa? " Yesu adawafunsa iwo. Ndipo anawauzanso kuti, mkati mwa mitima ya anthu mutuluka maganizo oyipa azachiwerewere, zakuba, zachigololo, kusilira, dyera, chinyengo, zakupha ndi bodza. Zonse zimenezi zimatuluka mkati mwa munthu ndikumupanga munthuyo kukhala wodetsedwa (7:21-23).

Choncho kusamba manja sikuyeretsa mitima yathu. Mulungu yekha ndiamene angatiyeretse ife mkati mwathu. Afarisi ena anakhulupilira miyambo ya chipembedzo m'malo modalira Mulungu. Ichi ndi chifukwa chake Yesu adawatcha iwo onyenga, poti anali kuwonetsa kwa anthu ubwino wongoyerekeza (7:6; Luka 11:37-54; Luka 12:1-3). Anthu sasowa kusunga malamulo akale achiyuda onena za zakudya zodetsedwa ndi zosadetsedwa (7:19). (Ayuda sanali ololedwa kudya mitundu ina ya nyama). Sichakudya ayi, koma zinthu zimene ife tiganiza ndi zimene ziri zofunika kwa Mulungu.

## MKAZI WA AMITUNDU KOMA WACHIKHULUPIRIRO

Yesu ananyamuka napita ku Turo mbali mwa nyanja ya mchere (7:24).Turo ndi Sidoni inali mizinda ya kale ndithu pagombe lanyanja yayikulu ya Meditereniyani. Anthu okhala kumeneko sanali a Yuda ayi. Anali amitundu, opembedza milungu ina. Turo unali pa mitunda makumi 40km ku nyanja ya Galileya. Yesu sanafune kuti anthu adziwe kumene iye anali komabe anthu anamzindikira. Mayi wina anamuwona Yesu namuyitana kuti akachiritse mwana wake wamkazi. Mayiyu anali wa amitundu amene a Yuda amene anawawona ngati agalu.

Lye adagwada pa mapazi a Yesu namudandaulira kuti amuthandize. "Baleka athange akhuta ana; pakuti sikwabwino kuti titenge chakudya cha ana ndi kutayira tiagalu" Yesu ananena naye. Yesu adatanthauza kuti adadza kudzaphunzitsa chowona cha ufumu wa kumwamba kwa mtundu wa chiyuda choyamba. Mayiyo ada dziwa zimene Yesu adali kutanthauza (Yohane 1:11; Mateyu 10:5, 6). Nthawi yopatsa mkate amitundu inali isanakwane (Marko 16:15).

Kodi Yesu anali kumufunsa mayiyu chiyani? " Chingathe chikhulupiro chako kupyola mitundu ndi zipembedzo ndi kudza kwa ine? Kodi uli nacho chikhulupiliro chokwanira kutha kuchiritsa mwana wako w'amkazi?

Mayiyo anayankha nati "Tingakhale tiagalu ta pansi pagome tikudya nyenyeswa za ana” (7:28). Apa mayiyo adasonyeza kuti anali nacho chikhulupiliro. Analibe kunyada komuletsa kudza kwa muyuda. Yesu adakondwa nako kuyankha kwa mayiyu ndipo anamuwuza kuti mwana wake wachiritsidwa (7:29).

Ufumu wa Mulungu ndi wa anthu onse ndipo mayiyu adapapatiza nawo ngakhale sanali muyuda. Lyeyu anali mwina, woyamba kutero muzindawu (Mateyu 8:13; 11.12).

Zachisoni kuti opembedza ambiri achiyuda sanakhulupilire mwa Yesu, koma amitundu ndi anthu wamba anali nacho chikhulupiliro mwa Yesu.

## YESU ACHIRITSA MUNTHU WOGONTHA NDI WOSAYANKHULA

Atachoka ku Turo. Yesu adayenda ulendo wozungulira kubwerera ku nyanja ya Galileya. Atayenda mitunda zana limodzi, anapeza munthu amene anali wogontha ndi wosayankhula. Yesu anamuchiritsa munthuyo chifukwa cha chikhulupiliro cha iwo amene anamutengera kwa iye.

**Kambiranani izi:**

1. Muganiza kuti Yesu ananeneranji kwa mayi uja motero asanachiritse mwana wake.
2. Mayi wa amitundu adamupempha Yesu madalitso otani?
3. Kodi mayiyu adakhulupirira chiyani mwa Yesu.
4. Mudziwa bwanji kuti mayiyu adamvetsa za Yesu kuposa a Yuda ena ambiri?
5. N'chifukwa chiyani Yesu sanachiritse mwana wa mayiyu nthawi yomweyo?
6. Kodi Yesu adachita ndi kunena zinthu zisanu ndi zitatu ziti kwa munthu wogontha uja (7:33-34)?
7. Kodi muganiza kuti Yesu adachitiranji zinthu izi zones asanamuchiritse munthu uja?

## KUCHIRITSA ANTHU WODWALA

'Kodi wina wa inu akudwala? ' Yakobo anafunsa pemphero loperekedwa mwa chikhulupiriro lingathe kuchiritsa munthu wodwala (Yakono 5:14-15).

Tchimo limadwalitsa. Ife tikhoza kudwala ndi nkhawa, ndi ntchito ndiponso matenda. Anthu ena amadwala mu ubongo wawo. Ena amadwala chifukwa cha ziwanda. Mulungu akhoza kuchiritsa matenda onse. Anthu wodwala ayenera kuwona kuti asowa kukhudza kwa Mulungu. Ayenera kupempha atsogoleri a mpingo, okhulupirira amene amadziwa za malonjezo a Mulungu. Awa ndi amene ali ndi mphamvu ndi ulamuliro wa Yesu (Mateyu 28:18).

Amenewa abwere ndi kuwapempherera wodwalawo ndi kuwadzoza mafuta mu dzina la Yesu Ambuye. Mafutawa ayimirira Mzimu Woyera. Lye ndi mphamvu ya Mulungu mu mpingo. Timapempha Mulungu kuti achiritse munthu odwala mdzina la Ambuye Yesu.

Timapempha kuti Ambuye achotse nthenda kapena nkhawa. Lye amachiritsa munthu amene iye afuna kuti achire. Amathanso kupereka chisomo, chikondi ndi mphamvu ya kupirira mu zowawa zawo. Paulo adafunsa Mulungu katatu kuti achize minga ya pathupi pake. Mulungu sanamuchiritse ayi. Adamuuza Paulo, Chisomo changa ndi chokwanira kwa iwe, pakuti mphamvu yanga iri yangwiro mu kufooka kwako (2 Akorinto 12:9).

## Kuwerenga Baibulo: Marko 8:1-38

## YESU APHUNZITSA ANTHU

Mu chaputalachi, akuphunzira aphunzira zambiri za iwo eni ndiponso za Yesu.

- Akuphunzira ali ndi chikhulupiriro chochepa ndi mitima yowuma (8:17-21).
- Petro anena kuti Yesu ndiye yani (8:29).
- Yesu awawuza za imfa yake ndi kuwuka kwake (8:31).

- Otsatira ake ayenera kusenza mtanda wawo ndi kumtsatira Yesu (8:34).
- Yesu anena za kubweranso kwake kwa chiwiri (8:38).

Khamu lalikulu linali kumvetsera pamene Yesu anali kuyankhula (8:1). Anthuwa atatha masiku atatu opanda chakudya. Kumeneku kunalibe malo ogulitsirako zakudya koma ophunzira anali ndi mikate isanu ndi iwiri.

Yesu anatenga mikate yawoyo anayidalitsa, nayinyema ndipo anawapatsa akuphunzirawo kuti awapatse anthuwo (8:6). Apanso Yesu anagwiritsa ntchito akuphunzira pochita zozizwa. Amuna pafupifupi zikwi zinayi, kudzaponso azimayi ndi ana anadya ndi kukwanitsidwa. Yesu atawabalalitsa anthu aja, iye pamodzi ndi akuphunzira adalowa mungalawa napita mbali ina ya nyanja ya Galileya.

Kumeneko, Afalisi adamufunsa za chizindikiro chochokera kumwamba (Luka 23:8). Adachita izi kuti amuyese iye, popeza adafuna kudzionera wokha mphamvu yake yayikulu. Analibe chikhulupiriro ndipo mafunso awo adafika pomutopetsa Yesu. Panalibe chizindikiro chidzapatsidwa kwa inu kupatula chizindikiro cha Yona, Yesu adawauza (8:12).

Pamene akuphunzira anali mungalawa kupita ku Betisida Yesu anati, "Yang'anirani, penyani kuti mupewe chotupitsa mkate cha a Farisi ndi chotupitsa mkate cha Herode (8:15). Akuphunzira sanamvetsetse chifukwa iwo adaganiza kuti Yesu anali kunena mawuwa pakuti iwo adayiwala kutenga mkate. Komatu Yesu adali kuwachenjeza iwo za tchimo ndi choyipa. "musalole kuti chikhulupiliro chanu chifanane ndi cha iwo, lye anatero. Mkate wa dziko lapansi ndi wosakhalitsa. Ndi Yesu yekha amene angatikhutise nthawi zonse. Lyeyu ndiye Mkate wa moyo.

Ku Betisida anthu ena adadza naye kwa Yesu munthu wa khungu. Iwo adamupempha Yesu kuti akhudze maso a munthuyo (8:22). Lyi ndi nthawi yokhayo imene Yesu adabwereza pofuna kuchiritsa munthu. Akuphunzira ake anali ngati munthu wa khunguyu. Iwo sanathe kuwonetsetsa nthawi yoyamba, zinthu zimene Yesu adaphunzitsa za ufumu wa kumwamba.

## PETRO AVOMELEZA KUTI YESU NDI KHRISTU

Yesu ndi akuphunzira anali kuyenda kudutsa mkati mwa midzi pamene iye adafunsa akuphunzirawo, Kodi anthu anena kuti ine ndine yani? (8:27) Lye adafuna kuti amve iwo zimene anganene, zimene iwo amakhulupilira. Iwo adayankha motere: "Ena amati ndinu Yohane M'batizi, ena amati ndinu Eliya ndipo ena amati ndinu m'modzi wa aneneri (8:28). Koma inu mumati ndine yani? Yesu adawafunsa (8:29).

Petro anayankha nati, "Ndinu khristu" Petro anali kutanthauza khristu, Mesiya, Mfumu imene Mulungu adalonjedza. Yesu adakondwa ndi yankho limeneri. "Kumvetsetsa uku sikudapatsidwe kwa iwe ndi munthu, koma Atate wanga wa kumwamba, " Yesu adamuwuza Petro.

## NJIRA YA MASAUTSO

Atayandikira mapeto akuphunzitsa kwake, Yesu adawuza akuphunzira ake za zomwe zitazamuwonekere. Lye anati adzasautsidwa mu zinthu zambiri ndiponso kuphedwa (8:31). Adalankhula nawo mwa chindunji osati mumafanizo. Lye anati adzaphedwa. Mwana wa munthu adzachotsedwa:

- Ndi anthu ake omwe
- Ndi akulu achipembedzo
- Ndi akulu ansembe wokhala nayo mphamvu.

Onse adzakuwa, "Mpachikeni! " Koma atapita masaiku atatu lye adzawuka kwa akufa. Petro adakhumudwa atamva izi. Anamutengera Yesu pambali ndi kumudzudzula, "Iyayi Ambuye", lye anatero, "Izi sizingachitike kwa Inu" (Mateyu 16:22).

Yesu anamuyang'ana Petro ndi akuphunzira ena onse. Lye anati, " Pita kumbuyo kwanga satana. Iwe sukuganizira (ndikunena) zinthu za Mulungu (8:33). Tiwona kuti mukamphindi kochepa Petro anasinthika, kuchoka pomvera Mulungu (Pamene anati ndinti Khristu) kufika pomvera satana.

Zimene Petro adanena apa ndizomwe Petro anali kufuna. Satana ndiye adalonga mawuwa mkamwa mwa Petro. Satana amatha kugwiritsa njira ina ili yonse kuletsa kapena kulepheretsa cholinga cha Mulungu, chofuna kupulumutsa amuna ndi akazi.

## SENZANI MTANDA WANU NDIPO TSATANI YESU

Petro sanafune kumutsatira Yesu ngati iyeyo anali kukaphedwa. Chonho Yesu adawachenjedza onsewo kuti akhoza kukhala akuphunzira, koma pali dipo lake. Wakuphunzira aliyense anayenera "kusenza mtanda" wake. Mtanda ndiye njira ya moyo. Aliyense ayenera kukonzekera kufa mu umwini (kutaya khalidwe la umwini, moyo wawo) ndikulandira chifuniro cha Mulungu m'moyo wawo.

Izi ndi zimene Petro anayenera kuchita.

Kwa ife akhristu, mtanda wa Khristu sichinthu chokongola ayi. Mtanda sichinthu cha golide chokowekedwa pa ukhufu. Mtanda wa Yesu ukuyimirira imfa. Kufa kumoyo wathu wakale pamene tinyamula mtanda wake wa Yesu, tikhala moyo kuti timutumikire Mulungu. Timachita zinthu zokhazo zimene zimakondweretsa Mulungu.

Mtanda uyimira kufa ku undekha, komanso uyimira moyo watsopano mkati mwathu.

Munthu wofuna kutsata Yesu ayenera kuzikaniza yekha. Lye ayenera kusiya zilakolako zake zadyera. Yesu anali kuchita izi munthawi yonse ya moyo wake. Yesu anasiya ulemelero ndi ulamuliro ndi kubwera pa dziko pano kudzachita zimene Atate (wake) anafuna (Afilipi 2:7-8). Pano akuyitanira onse

omutsatira kumoyo womwewo. Anasiya zense kufunafuna ndi kupulumutsa otayikawo.

Pamene Yesu anawawuza akuphunzira ake kunyamula mtanda ndi kumtsata iye (8:34) analinso kuganizira za nthawi imene adzakhomeredwe pa mtanda kunja kwa mzinda wa Yerusalemu. Yesu akufuna omutsatira amukhazike iye woyamba pa moyo wawo, ndikufalitsa uthenga wa bwino (8:35). Ena akhbza kutaya moyo pogwira ntchitoyi. Kodi ndife okonzeka kutero?

Yesu akunenanso zakubwera kwake kwa chiwiri (8:38). Tinenanso za zimene zidachitikira Yesu asanafe komanso atawuka kwa akufa.

**Kambiranani izi:**

1. Yesu adafunsa mafunso awiri ati aoneana za iye mwini (8:27-29). Yankho lanu ndilotani?
2. Kodi tingachitenji ngati tikulephera kuchotsa undekha (8:35)?
3. Kodi cha mtengo waukulu kuposa thupi la munthu nchiyani (8:36)?
4. Mwina tikuwopa kutaya moyo wathu ngati titsatira yesu. Koma kodi tiyenera kuwopa kwambiri chiyani (8:38)?

**Published by:**
Manna Publications (UK)

**In association with:**

**Typeset by:**
MissionAssist (UK)

**Distributed by:**

**Printed by:**

**Mulungu watheketsa kuti mabuku ofotokoza Baibulo a Manna asindikizidwe ndi kufalitsidwa mu:**

Angola, Armenia, Benin, Bulgaria, Burkina Faso, Burundi, Cambodia, Cameroon, Chad, Congo Dem. Rep. (Kinshasa and Katanga), Congo Rep. (Brazzaville), Egypt, Equatorial Guinea, Ethiopia, Ghana, Guatemala, Haiti, India, Ivory Coast, Kenya, Kosovo, Liberia, Malawi, Mali, Mexico, Mongolia, Mozambique, Myanmar, Nepal, Niger, Nigeria, Pakistan, Rwanda, Serbia, Sierra Leone, South Africa, Sudan, Swaziland, Tanzania, Togo, Uganda, Zambia, Zimbabwe

**ndipo m'zinenero 43 kuphatikizapo 2 za akhungu**

Pitani pa webusayiti yathu pa **www.manna-publications.org.uk** kuti mupeze ndemanga zambiri za Baibulo m'Chingelezi chosavuta, Chifulenchi, Chipwitikizi ndi Chisipanishi. Chonde titumizireni kudzera pa webusayiti yathu kuti mudziwe zilankhulo zina.

Wogwirizana ndi **Avail**, UK adalembetsa zachifundo 1017386

Gulu la makolo la Manna Publications (USA): www.mannapublications.org

# UTHENGA WABWINO WOLEMBEDWA NDI MARKO
## Marko Gawo 1: Mutu 1 mpakana 8

| | |
|---|---|
| • **Ubatizo wa Yesu**<br>• **Ophunzira a Yesu**<br>• **Zozizwitsa za Yesu** | • **Chifundo cha Yesu**<br>• **Miyambi ya Yesu**<br>• **Kupulumutsidwa ku Mizimu Yoipa** |

**BUKU LOYAMBA ILI** lolembedwa ndi mmishonale Fred Morris limatiuza za masiku oyambirira a utumiki wa Yesu padziko lapansi. Uthenga Wabwino wa Marko umafotokoza za ziphunzitso Zake ndi machiritso Ake. Limatiuza tanthauzo la kukhala wotsatira wa Yesu masiku ano. Zimamanga chikhulupiriro chathu kuti tichite ntchito yake. Imatikonzekeretsa kulalikira Uthenga Wabwino wa Ambuye wathu Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu ndi Mesiya wa Isiraeli. Iye anabwera kudzakhululukira machimo ndi kusintha moyo wathu kwamuyaya.

**MANNA PUBLICATIONS** amasindikiza timabuku tating'ono tofotokoza za Baibulo lolembedwa ndi Fred Morris. Kwa zaka zambiri Fred, ndi mkazi wake Lorna, ankayendayenda padziko lonse akuphunzitsa ndi kulalikira. Mabuku ake ndi osavuta kuwerenga, kumva komanso kumasulira m'zilankhulo zina. Amapereka chiphunzitso choyambirira chogwiritsa ntchito panokha kapena kuphunzira pagulu, kuphatikiza zolemba zina za ophunzira Baibulo, aphunzitsi ndi abusa.

**MABUKU** amenewa adzakuthandizani kumvetsa choonadi chochokera kwa Mulungu Wamphamvuyonse. Iye amalambiridwa ndi mamiliyoni a Ayuda ndi Akristu padziko lonse lapansi. Mabuku amenewa adzakuthandizaninso kuti mulandire chipulumutso ndi moyo wosatha kudzera mwa Mwana wa Mulungu, Yesu Khristu yemwe ndi Mesiya wa Isiraeli. Adzakuthandizani kulankhula za chikhulupiriro chanu mwa Mulungu ndi kupemphera kwa Iye. Iwo adzakuthandizani kukutsogolerani ku njira yolakwika m'moyo. Iwo adzakuthandizani kukhala ndi moyo wokondweretsa Mulungu kudzera mu chikondi ndi mphamvu ya Mzimu Wake Woyera. Izi zidalonjezedwa kwa okhulupilira onse pambuyo pa kupachikidwa ndi kuuka kwa akufa kwa Yesu amene amakhulupirira kuti ndi Mwana wa Mulungu.

**TIMAPEMPHERA** kuti mukhale ndi mtendere watsopano ndi cholinga m'moyo pamene mudalira Mulungu, kuwerenga Baibulo ndi kugwiritsa ntchito ndemangazi. Pamene mukuphunzira choonadi cha m'Chipangano Chakale ndi Chatsopano chochokera kwa Mulungu, ganizirani zimene Yesu


**Manna Publications**

**MAZIKO A NDEMANGA ZA BAIBULO**

**Chinsinsi cha Ufumu WA Mulungu pakati pathu (Marko 4:11)**